6-Yesu anayankha kuti, “Ine ndine njira, chowonadi, ndi moyo. Palibe munthu amene adza kwa Atate, koma mwa Ine.

-Yesu analankhulanso kuti Iye ndi Njira yopitira kwa Mulungu.
-Ngati mukufuna kuyidziŵa njira yopitira kwa Mulungu, mungotembenukira kwa Yesu.

-Yesu analankhulanso kuti Iye ndi Chowonadi.
-Ngati mukufuna kuchidziŵa chowonadi, mungotembenukira kwa Yesu.

-Yesu analankhula kuti Iye ndi Moyo.
-Ngati mukuwufuna moyo osatha, mungotembenukira kwa Yesu.

-Palibe amene amapita kwa Mulungu Atate osadzelera mwa Yesu.



PHUNZIRO LA 60

1. Kodi ndi funso lotani limene Yesu anaŵafunsa ophunzira ache?
-Yesu anafunsa kuti, “Kodi anthu akuti Ine ndani?”

2. Kodi ophunzira a Yesu anayankha kuti chiyani?
-Anthu ena ankaganiza kuti Yesu anali Yohane M’batizi
-Anthu ena ankaganiza kuti Yesu anali Eliya.
-Anthu ena ankaganiza kuti Yesu anali m’modzi mwa aneneri amene anadzuka kuchokera ku imfa amene anadzuka kuchokera ku imfa.

3. Kodi Yesu anali Yohane M’batizi, Eliya, kapena m’modzi mwa aneneri amene anawuka kuchokera ku imfa?
-Ayi.

4. Kodi nanga Peturo anayankha kuti chiyani?
-Peturo anayankha kuti, “Inu ndi Kilisitu.”

5. Kodi ngati ife sitikukhulupilira kuti Yesu ndi Mulungu Mpulumutsi, tingapulumutsidwe?
-Ayi.

6. Kodi Yesu anaŵaphunzitsa chiyani ophunzira ache za zimene zinkadza?
-Yesu anaŵaphunzitsa kuti akuluakulu a anthu adzamupha Iye, koma adzawukanso kuchokera kwa akufa patatha masiku atatu.

7. Kodi chinachitika kwa Yesu ndi chiyani pa phiri paja?
-Yesu anasanduka pamaso pa Peturo, Yohane ndi Yakobo.

8. Kodi zikutanthawuza kuti chiyani ndi kusanduka kwa Yesu?

-Zikutanthawuza kuti Mulungu amene anali mkati mwa Yesu anawonekera kunja.

9. Kodi Eliya anali ndani?
-Eliya anali mneneri wa Mulungu amene anabwera pa dziko la pansi Yesu asanabadwe pa dziko la pansi

Mu zaka zambiri zapitazo, Eliya asanafe, Mulungu anamutenga iye ndikupita naye kumwamba.

10. Kodi Mose anali ndani?
-Mose anali munthu amene anaŵatsogolera a Isirayeli poturuka mu dziko la Iguputo.

-Mu zaka zambiri zapitazo, Mose anafa, ndipo Mulungu anawutenga mzimu wache ndikupita nawo kumwamba.
-Chifukwa chakuti Eliya ndi Mose ankakhulupilira mwa Mulungu, akukhalabe ndi Mulungu kumwamba mpaka lero.

11. Kodi Eliya ndi Mose anabweranso bwanji pa dziko la pansi pano?
-Mulungu Atate anaŵatumiza iwo kuchokera kumwamba kudzalankhulana ndi Yesu.

12. Kodi chifukwa chiyani Mulungu Atate anafuna kuti Eliya ndi Mose adzalankhulane ndi Yesu?
-Mulungu Atate ankafuna kuti Mose ndi Eliya amulimbikitse Yesu pa imfa imene ankadza kwa Iye.

13. Kodi Mulungu Atate analankhula chiyani kwa ophunzira a Yesu?
-Mulungu Atate analankhula kuti Yesu anali Mulungu Mpulumutsi, ndipo ophunzirawo ayenera kumumvera Iye.

-Ayuda ambiri m'masiku a Yesu nali abusa a ziweto.



-Kodi mbala imene imadza kudzangoba, kupha ndi kuwononga ndi ndani?
-Satana.

-Kodi chifukwa chiyani Yesu anabwera?
-Yesu anadza kudzatipatsa ife moyo, ndiponso kudzatipatsa ife moyo osatha.

-Yesu ndi Satana ndi osiyana.

-Satana anadza kudzaba, kudzapha ndi kuwononga nkhosa.
-Yesu andza kudzapereka moyo kwa nkhosa.

-Kodi china chimene analankhula Yesu nd chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Yohane 10:11

11-[Yesu anatinso kuti] "Ine ndine M'busa Wabwino; m'busa wabwino ataya moyo wache chifukwa cha nkhosa."

-Yesu analankhula kuti Iye anali M'busa wabwino.

-Yesu analankhulanso kuti anazikonda nkhosa zache ndipo anali okonzeka kufa chifukwa cha nkhosazo.

-Yesu analankhula kuti anali akonzeka kufera nkhosa zache kuti azipulumutse ku tchimo, imfa ndi Satana.

-Kodi china chimene analankhula Yesu nd chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Yohane 14:6

kwa Mulungu.
-Limenelo ndi bodza lamkunguniza.

-Anthu ena amalankhula kuti pali njira ya makolo athu yopitira kwa Mulungu.
-Limenelinso ndi bodza lamkunguniza.

-Yesu analankhula kuti Iye ndi njira yokhayo imene ife tingapulumukire.

-Kodi m'masiku a Nowa, Mulungu anamulamula Nowa kuti amange makomo angati a chombo chija?
-Limodzi lokha.

-Kodi khomo limodzi lokha la Nowa likutikumbutsa ife chiyani za Yesu?
-Ngati m'mene linalili khomo limodzi la chombo cha Nowa, chomchonso Yesu ndilo khomo lokhalo la ku moyo osatha.

-Ngati m'mene anapulumukira ku imfa anthu amene analoŵa m'chombo muja pogwiritsa nthito khomo limodzi, chomchonso anthu amene
akukhulupilira mwa Yesu adzapulumutsidwa ku mfa.

-Kodi china chimene analankhula Yesu nd chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Yohane 10:10

10-[Yesu anatinso kuti] "Mbala imangodza kudzaba , kupha ndi kuwononga. Ine ndadza kuti inu mupeze moyo, ndiponso moyowo ukhare
ochuruka."

-Yesu analankhulanso kuti mbala imadza kudzaba, kupha ndi kuwononga basi.



-Abusawo ankayang'anila nkhosa zambiri.
-Chifukwa chakuti malo ambiri a ku Isirayeli anali owuma, kunali kovuta kuti abusawo apeze msipu wodyetsera nkhosa zawo.

-Chomcho abusawo ankayenda mtunda wawutali kuti apeze sipu okwanira odyetsera nkhosa zawozo.

-Chifukwa chakuti abusawo ankayenda mitunda yayitali-yitali, iwo ankagona m'malo osiyanasiyana ndi nkhosa zawozo.

-Chifukwa chakuti kunali mbala zambiri zimene zinkaba ziweto zawozo ndiponso nyama zolusa zimene zinkagwira nkhosa zawozo, abusawo ankayenera kukhwimitsa chitetezo cha ziwetozo usiku.

-Kodi abusawo ankateteza bwanji nkhosazo usiku?
-Usiku usanafike, abusawo ankamanga linga la miyala kapenga minga mozungulira pa malopo ndipo ankayika khomo limodzi.

-Lingalo likatha, abusawo ankazikusila nkhosa zawozo mkati mwa lingalo ndipo iwo ankagona pabwalo.

-Kodi chifukwa chiyani abusawo ankagona pa bwalo?
-Kuti ateteze nkhosa zimene zinkakhala zili mu lingalo.

-Chifukwa chakuti abusawo ankagona pabwalo, ankakhala ngati khomo la lingalo.

-Palibe mbala kapena nyama yolusa imene inkaloŵa mu lingalo isanakumane kaye ndi mb'usa.

-Tsiku lina Yesu anayambanso kuŵaphunzitsa anthu.

Tiyeni tiŵerenge Yohane 10:7

7-[Chomcho Yesu anatinso kuti] “Ine ndine khomo la nkhosa.”

-Kodi Yesu ankatanthawuza chiyani pamene ankalankhula kuti Iye ndi khomo la nkhosa?
-Yesu ankatanthawuza kuti Iye ndi Njira imene ife tingapulumukire ku imfa.

-Ngati m’mene m’busa ankakhalira khomo kuti apulumutse nkhosa zache ku imfa, chomchonso Yesu ndi khomo lotipulumutsira ife ku imfa.

-Ngati m’mene nyama zolusa zinkakhalira kunja kwa linga, kuyembekezera kuti mwina zingagwire nkhosa ndi kudya, chomchonso tchimo
ndi imfa zikuyembekezera kuti zidye anthu onse.

-Ngati m’mene mbala zinkayembekezelera kunja kwa linga kuti mwina zingabe nkhosa, chomchonso Satana ndi ziwanda zache
akuyembekezera kuti abe anthu onse.

-Ngati mbala, Satana wakhala akuba makolo anu kwa zaka zambiri.

-Satana amaba anthu ndi cholinga chakuti aŵawononge.

-Yesu amakonda nkhosa zache ngati m’mene abusa a nkhosa amakondera nkhosa zawo.

-Kodi nkhosa za Yesu ndi ndani?
-Anthu amene akudziŵa kuti tchimo lawo likuyitana imfa, ndipo akupempha Yesu kuti aŵapulumutse.



-Yesu akufuna kutipulumutsa ku tchimo ndi imfa.
-Yesu akufuna kutipulumutsa ife kuchokera kwa Satana ndi ziwanda zache.

-Kodi china chimene analankhula Yesu nd chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Yohane 10:8

8-[Yesu anati] “Onse amene anadza Ine ndisanadze ali akuba, ndipo olanda, koma nkhosa sizinaŵamvere iwo.”

-Yesu asanabadwe pa dziko la pansi, anthu ena ankapita kwa Ayuda ndikumakaŵawuza kuti iwowo ndi Apulumutsi.

-Yesu analankhula kuti anthu ameneŵa anali ngati mbala ndiponso olanda.

-Kodi china chimene analankhula Yesu nd chiyani?

Tiyeni tiŵerenge Yohane 10:9

9-[Yesu anatinso kuti] “Ine ndine khomo; Ngati wina aloŵa kupitira mwa Ine, adzapulumutsidwa, adzaloŵa, ndipo adzaturuka, nadzapeza
chakudya.”

-Yesu analankhula kuti Iye ndi njira yokhayo imene ife tingapulumukire.

-Ngati m’mene inkakhalira njira imodzi ya linga la nkhosa, chomchonso Yesu ndi khomo lokhalo limene tingaloŵere ku moyo osatha.

-Anthu ena amalankhula kuti pali makomo ambiri opitira